



ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027

UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo

CHIKWAWA


DISTRICT

Mwachidule

Nyengo ya Dzinja ya 2026-2027 kudzakudzidwa ndi El-Nino wa mphamvu. El Nino ndi kutentha kopyola muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific zomwe zimakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse.


Boma la Chikwawa likuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuchepera apo mu nyengo ya dzinja la 2026/2027.

October 2026



Madera ambiri kudzagwa mvula yosapitilira 30mm imene ndi mlingo okhazikika komanso kuchepera apo. Mvula ya Chizimalupsya ikuyembekezereka m'mwezi umenewu imene itha kudwabwera ndi mphepo yamkuntho komanso mabingu..


November 2026



Mlingo wa mvula okhazikika okwanira 50mm mpaka 100mm ukuyembekezeka m'madera ambiri m'mweziwu.

Mvulayi idzatsagana ndi ziphaliwali komanso mphepo ya mkuntho


December 2026



Madera ambiri akuyembekezeka kudzalandira mvula yopyola mlingo wokhazikika yokwana 150-220mm m'bomali mweziwu.


Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kudzayamba sabata lachiwiri m'mweziwu.

January 2027



Mvula yamlingo okhazikika yokwana 200mm ikuyembekezeka m'madera ambiri pamene madera ena a TA Ngabu, ndi TA Lundu akuyembekezedwa kudzalandira mvula yosapitilira 150mm. Kuthekera kwa ng'amba yofika masabata awiri m'madera ena


February 2027



Mvula yochepera pa mlingo okhazikika ikuyembekezeka m'madera ambiri m'bomali, wa pakati pa 100mm ndi 120mm m'mweziwu.


Komabe pali kuthekera kwa ng'amba yofika masabata awiri m'madera ena.

March 2027



Mvula ya mlingo okhazikika kapena yoposera apo ya pakati pa 70mm ndi 140mm ikuyembekezeka kudzagwa m'madera ambiri m'bomali.

April 2027



Mlingo wa mvula wa pakati pa 20mm ndi 50mm umene ndi okhazikika ukuyembekezeka kudzagwa m'bomali mweziwu.

Dzinja likuyembekezeka kufika kumapeto sabata loyamba la mwezi umenewu.

DZINJA MWACHIDULE

Kuyamba kwa mvula yokhazikika

Ikuyembekezereka sabata lachiwili mu December 2026

Ng'amba

Pali chiopsyezo cha ng'amba ya masabata awiri miyezi ya January ndi February


Kutalika kwa nyengo yadzinja

Dzinja lidzakhala masiku apakati pa 120 ndi 130

Mathero a mvula dzinja

Sabata loyamba la April 2027

MONTH	NORMAL RANGE	FORECAST
OCT	1.8	30.4
NOV	38.4	92.2
DEC	99.5	182.8
JAN	138.4	227.6
FEB	99.9	200.4
MAR	51.2	117.2
APR	22.2	47.5



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo



For further information contact:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.



+265 991 69 00 61



metdept@metmalawi.gov.mw



www.metmalawi.gov.mw